

Kodi Pachithunzipa Pakusoweka Chiyani?

Werengani 1 Mbiri 16:1, 2, 4-10. Kenako yang'anani chithunzichi. Tchulani zinthu zimene zikusowekapo. Lembani mayankho anu m'munsimu. Malizitsani kujambula chithunzichi polumikiza timadonthoto, ndipo chikongoletseni ndi chekeni.

- 1.....
- 2.....
- 3.....

KAMBIRANANI: Kodi Yehova Mulungu amamva bwanji tikamaimba ngati njira yomulambira? N'chifukwa chiyani mukuyankha choncho?

ZOKUTHANDIZANI: Werengani 2 Mbiri 5:13, 14; Aefeso 5:19. Kodi mungatchule nkhani zina za m'Baibulo zomwe anthu anaimba polambira Mulungu? **ZOKUTHANDIZANI:** Werengani Ekisodo 15:1-20; Maliko 14:26; Machitidwe 16:25. Kodi n'chiyani chingakuthandizeni kuti muziyesetsabe kuimbira Yehova ngakhale kuti ndinu wamanyazi kapena ngati mumaona kuti simutha kuimba? **ZOKUTHANDIZANI:** Werengani Salimo 33:1-3.

ZOTI BANJA LICHITIRE PAMODZI: Aliyense wam'banjamo asankhe nyimbo yotamanda Yehova imene amaikonda. Ndiyeno, muphunzirire pamodzi nyimbozo mpaka mutazidziwa bwino.



YAMBIRANI APA

THERANI APA

Nkhani zina zakuti, "Zoti Banja Likambirane" mungazipeze pa adiresi yathu ya pa Intaneti ya www.jw.org/cn

1. Chithema chosungiramo likasa.
2. Zeze. 3. Lipenga.